

Danieli : 7:24-28

Mutu : Kumasulira kwachirombochachinayi

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero, Ambuye atitsogolere ndi mau apa Yesaya 29:15, amene akuti, “Tsoka kwa iwo amene afunitsakubisira Yehova uphungu wawo, ndi ntchito zawo ziri mumdima ndipo amati ndani ationa ife? Ndani atidziwa ife?”

Mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 7:13-23, m’mene timaunika za tanthauzo la zirombo zinayi. Ndipo lero pa Danieli 7:14-28, tikambirana za kumasulira kwachirombochachinayi.

14.Kunena za nyanga khumi, m’ufumu uwu adzauka mafumu khumi, ndi pambuyo pawo idzauka yina; iyoidzasiyana ndi oyamba aja, nidzachepetsa mafumu atatu.

Pano mngelo wa Mulungu akupereka tanthauzo lomveka bwino mu verse 23, momwe akunena kuti chirombochachinayi, chikuimira ufumu wachinayi, wokhazikitsidwa pansi pano. Uwu, ndiufumu womwe udzakhala wosiyana kotheratu ndi mafumu ena onse a m’mbuyomo chifukwa ndiwo udzatenga ulamuliro padziko lonse

lapansi mwankhaza. Kunena kuti pamene ufumu uwu, uzidzakhazikitsidwa, udzakhala ukuthyola ndi kuononga maufumu ena.

Tere, nyanga khumi za m' masomphenya pa verse 24, ndizo zinaphuka kuimira mafumu khumi a ufumu wa Roma. Mwanjira ina tikunena kuti ufumu wa Aroma ndiwo umene tirimo lero lino m' masiku otsiriza ngakhale kuti sukuonekera poyera. Koma mafumu khumi amene alimu ufumu umenewu ndiwo amene anagawikana m' chaka cha A.D. 456, umene ndi ufumu wa British, a Saxon, a Frank, a Burgandi, a Visigoth, a Suevia ndi Alane, a Vandalo, Alimane, a Ostrogoth ndi a Greek. Ufumu uwu, ndiwo ukugwirizana ndi zala khumi zijazikupezeka pa Danieli 2:41, zomwe zikuimira ufumu womwe ukunenedwa pa Chibvumbulutso 13:1, pamene akuti, "Ndipo ndina imirira pamchengawanyanja. Ndipo ndinaona chirombo chirimkudurukam'nyanja, chakukhala nazo nyanga khumi, ndi mitu isanu ndi iwiri ndi pa nyanga zake nduwirazachifumu khumi ndi pamitu pake maina amwano." Ndiye mngelo akumasulira kuti awa ndiwo maufumu amene akudza m' tsogolo monga akutsimikiza pa Chibvumbulutso 17:12, pamene

akuti, “Ndipo nyanga khumi udazona ndiwo mafumu khumi, amene sanalandire ufumu; koma alandira ulamuliro ngati mafumu ora limodzi, pamodzi ndichirombo.”

Wokondedwa anzanga apaulendo nkhani iyi, ikulinga pakuti mafumu onse khumi anauka panthawi yawo onse pamodzi, koma ufumu wa wokana Kristu ndiwo udzaturukapawokhanudzaononga mafumu atatu mwa mafumu khumi aja. Ndiye tikunena kuti monga mafumu ena aja anali ndi atsogoleri ake, momwemonso ufumu wachinayiwu, mtsogoleri wake ndiye wokana Kristu. Kunena kuti mfumu iyi, sidzangodzimveka dzina la Kristu lokha, koma kumukana Yehova ndi mwana wake yemwe. Iyi ndinkhani yomwe 1 Yohane 2:22, akunena kuti, “Wabodza ndani, koma iye wakanayo kuti Yesu siyali Kristu? Iye ndiye wokana Kristu, amene akana Atate ndi Mwana.”

Kutsimikiza kunena kuti pakati pa mafumu awa, padzabukanso ufumu wina. Iyi, ndiyo nyangayaing’ono, yomwe inaphuka pamutu womwewo, koma inaphuka pambuyo pa nyanga zina khumi. Uwu, ndiwo ufumu womwe ukuonekawaung’ono komanso wopanda mphamvu koyambirira. Ufumu uwu, ndiwo umene

udzakulamphamvu kotero kuti udzakhozakuphwasula ufumu wina utatu. Kutsimikiza kuti ufumu uwu, udzapondereza mafumu ena atatu, monga akunena pa Danieli 7:24, kuti, “idzachepetsa mafumu atatu mwa mafumu khumi aja.”

Kutanthauza kuti mfumu yachinayi, ndiyoidzakhala mtsogoleri wankhaza padziko lonse lapansi. Ichi, ndicho chithunzi chomwe tikuchiona pa Chibvumbulutso 13:7, pamene akuti, “Ndipo anachipatsa icho kuchita nkondo ndi oyera mtima, ndi kuwalaka; ndipo anachipatsa ulamuliro wapa pfuko liri lonse, ndi anthu ndi manenedwe ndi mitundu.” Kutsimikiza kuti mtsogoleri uyu, ndiye wotsutsa Kristu, amene akutchulidwa munthu wauchimo, amene adzalamulira dziko lapansi m’nthawi ya chibvuto chachikulu, ndi nthawi ya zaka zisanu ndi ziwiri.

15. Nidzanena mau akutsutsana ndi Wamwambamwamba, nidzalemetsaopatulika a Wam’mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo; ndipo adzaperekedwa m’dzanja lake mpaka nthawi imodzi ndi nthawi zina ndi nthawi yanusu.

Pano pali nkhanani yakuti nyangayaing'ono ndi yochitira Mulungu mwano. Kutanthauza kuti ufumu wachinayi ndiwo wotsutsana ndi Mulungu. Tamvani mau apa Chibvumbulutso 13:5-6, akunena kuti, "Ndipo anachipatsa icho m'kamwa molankhula zazikuru ndi zamwano; ndipo anachipatsa ulamuliro wa kutero miyezi makumi anayi ndi iwiri. Ndipo chinatsegula pakamwa pake kukanena zamwano pa Mulungu, kuchitira mwano pa Mulungu, kuchitira mwano dzina lake ndi chihema chake ndi iwo akukhala m'Mwamba."

Kutsindika kunena kuti chizindikiro chimodzi cha wotsutsa Kristu ndi chakuti amakana Mulungu ndi Kristu yemwe. Ndipo tanthauzo lina ndiye amene amayeseza kapena kutsaza Kristu m'machitidwe ake. Ndiye tikunena kuti zirombo ziwiri zomwe zikutchulidwa m'chapter 13, cha Chibvumbulutso zikuonetsa makhalidwe awiriwa ya wotsutsa Kristu. Kunena kuti wotsutsa Kristu ndiwo wotsutsa Mulungu komanso wonyoza Mulungu. Kachiwiri ndiye mneneri wabodza, amene amayeseza Kristu ndi cholinga chofuna kumakopa anthu mu ufumu wake. Kutsindika kuti wokana Kristu amaonetsa maonekedwe a nkhusa, koma alim'mbuluatabvalachikopa cha

nkhosa. Kutsimikiza mau apa 1 Yohane 2:22, amene akuti, “Wabodza ndani, koma iye wokanayo kuti Yesu siyali Kristu? Iye ndiye wokana Kristu, amene akana Atate ndi Mwana.”Koma taonani kuti panthawi yoikika, akunena kuti adzamuchotsera mphamvu yake ndi kumuonongakotheratu.Tsono nkhani ikuti Leronso alipo anthu ambiri amene amaonetsa moyo wachikristu, koma mumtima mwawo adamukana kale Mulungu ndi Mwana wake. Mwanjira ina awa, ndiwo anthu onyenga, amene Mulungu adzawaonongakotheratu, pamene tilowa m’chiweruzochotsiriza.

Tsono m’chitidwe wina wa wokana Kristu ndiwo kudzikweza. Kutanthauza kuti amadziyikapamzere umodzi ndi Mulungu, kapena amadzitenga kuti amafanana ndi Mulungu.Pachifukwa chimenechi amadzipatsa yekha mayina aulemu ndi ulemerero. Kunena kuti amadziika kuti ndiye woyera ngati Mulungu, kotero kuti amanena kuti ali ndi mphamvu yokhululukira tchimo.

Mngelo akumasuliranso kuti wokana Kristu ndiye amene adzazuza ndi kuononga wokhulupirira mwanjira yowapha ndi cholinga chofuna kuchepetsa chiwerengero chawo. Iyi, ndiyo nkhani yomwe Yohane pa Chibvumbulutso 11:8, akunena kuti, “Ndipo

mitemboyawo idzakhala pakhwalala mudzi waukuru, umene utchedwa, ponena zachizimu, Sodoma ndi Aigupto, pameneponso Ambuye wawo anapachikidwa.”Kunena kuti ichi, ndichifukwa chake anthu wokhulupirira akhala akusautsika kwambiri ndi wokana Kristu, kuchokera pachiyambi mpaka lero lino.

Wotsutsa Kristu amaganiza kuti ali ndi mphamvu yosintha nthawi, kuchotsa kapena kuonjezerapo malamulo a Mulungu. Kutsimikiza kuti amakhala ndi chilakolako chachikulu chofuna kuchita zimenezi. Tere ndichifukwa chake akutsaza Yehova pa Danieli 2:21, pamene akuti, “Pakuti amasanduliza nthawi ndi nyengo, achotsa mafumu, nalonga mafumu, apatsa anzeru nzeru ndi chidziwitso kwa iwo okhoza kuzindikira.” Ndiye mwa mau amenewa tipeza kuti wokana Kristu amakhoza kusintha nyengo, miyambo yachipembedzo, kupatula masiku ena kuti akhale wopatulika pamwezi ngakhale pasabata.

Tsono mngelo akunenetsa kuti ngakhale wokana Kristu ali ndi m’chitidwe umenewu, adzaperekedwa m’dzanja la Mulungu patapita zaka zitatu ndi theka. Uku, ndiko kumapeto kwa nthawi yachibvuto chachikulu nthawi yomwe wokana Kristu adzakhala ndi

ulamuliro pansi pano monga mwa mau apa Chibvumbulutso 13:5, amene akuti, “Ndipo anachipatsa icho m’kamwa molankhula zazikuru ndi zamwano; ndipo anachipatsa ulamuliro wa kutero miyezi makumi anayi ndi iwiri.”

16.Koma woweruza mlandu adzakhalako, ndipo adzachotsa ulamuliro wake, kuutha ndi kuononga kudikira chimariziro.

Tsopano womasuliraakutsimikiza kufunika kwamasomphenya pamene akufotokonzero za chiweruzo pachirombochachinayi pamodzi ndi mtsogoleri wake pakuchotsa ulamuliro wake ndi kuuononga kufikira chimariziro. Kutanthauza kuti pamene ufumu wachinayiudzaonongekakotheratu, ndiye kuti ulamuliro pa ufumu umenewu udzakhala m’manja mwa ana a Wam’mwambamwamba. Tsono pamene tinena kuti ulamuliro udzaperekedwakwa ana a Mulungu, sizikutanthauza kuti Mwana wa Mulungu alibe mphamvu yolamulira ayi, koma kuti ana a Mulungu adzakhala ndi mwayi wotumikiramufumu umenewu, kusiyana ndi momwe iwo anali kusautsidwa. Ichi, ndichimene akunena Danieli pa verse 14, pamene akuti, “Ndipo anampatsa ulamuliro ndi ulemmerero ndi ufumu kuti anthu onse ndi mitundu yonse ya anthu ndi a

manenedwe onse amtumikire; ulamuliro wake ndi ulamuliro wake sudzaonongeka.” Kutsimikiza kuti ufumu uwu, ukusiyana ndi maufumu a m’mbuyomu, amene anathamwadzidzipachiweruzo cha Mulungu nakhazikitsa ufumu wake umene ndiufumu umene sudzatha nthawi yonse, momwe mphamvu ndi ulamuliro wonse ndi anthu adzatumikira ndi kumvera Mulungu. Iyi, ndiyo nkhani ija adanena Ambuye Yesu pa Mateyu 19:28, pamene adati, “Indetu, ndinena kwa inu, kuti inu amene munanditsata Ine, m’kubadwanso, pamene Mwana wa munthu adzakhala pa chimpando cha ulemerero wake, inunso mudzakhala pa mipando khumi ndi iwiri, kuweruza mapfuko khumi ndi awiri a Israyeli.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano ndifuna muone kufunika kopereka ulemu kwa iwo amene amaopa Ambuye. Kutsindika kunena kuti ngakhale lero aoneke onyozeka motani m’maso mwanu ndi mwanga, koma ndiwo ana a Wam’mwambamwamba, amene akhala pafupi komanso kukondedwa ndi Mulungu. Awa, ndiwo amene adzatumikira panthawi yachiweruzo.

Tsono ntchito yochotsa ndi kukhazikitsa ulamuliro m’manja mwa ana a Mulungu idzachitika ndi ulamuliro wa Mulungu, monga

momwe amachitira oweruza atakhala pampando wachifumu. Mwanjira ina tikunena kuti Mulungu tate, kudzera mwa Kristu adzakhala pampando wakuweruza mozunguliridwa ndi angelo, ndi kupereka chilango kwa wokana Kristu. Kutanthauza kuti, iyi ndi ntchito yopereka chilango kwanyangayaing'ono, yomwe ndi wokana Kristu. Ichi, ndichimene Paulo anali kunena pa 2 Atesalonika 2:8, pamene anati, “Ndipo pamenepo adzabvumbulutsidwawosayeruzikayo, amene Ambuye Yesu adzamthera ndi Mzimu wa pakamwa pake, nadzamuononga ndi maonekedwe a kudza kwake.”

17. Ndipo ufumu ndi ulamuliro ndi ukulu wa maufumu, pansi pa thambo lonse, zidzapatsidwa kwa anthu a opatulika a Wam'mwambamwamba; ufumu wake ndiwo ufumu wosatha, ndi maiko onse adzamtumikira ndi kum'mvera.

Ndiye womasulira akunenetsa kuti pamene ufumu wachirombochachinayi udzachotsedwa kwa wokana Kristu, amene ndiyo nyangayaing'ono, ana a Mulungu, amene ndi wochokera kumitundu yonse ya anthu padziko lapansi, adzapatsidwa mphamvu ndi ulamuliro ndi kutumikira Mulungu padziko lonse

lapansi ndi kungsi kwathambo. Kutsimikiza kuti panthawi imeneyo ulamuliro wonse wa mafumu a dziko lapansi, udzakhala wa Ambuye Yesu ndi onse woyera mtima, amene adzakhala mafumu kapena kuti nduna zake. Awa, ndiwo anthu amene adzasangalala ndi kukondwa m'malamulo ndi kukhala muufulu m'chipembedzo mosazunzikanso. Kutsimikiza kuti ufumu wa Mfumu Mesiya, ndiwo wosatha, umene udzakhala kufikira mibadwo mibadwo.

Tsono tiyenera kumvetsa kuti ulamuliro uwu, siulamulirowa ufumu wapansi pano ayi. Uwu, ndiwo ulamuliro wamoyo wauzimu pa wokhulupirira onse. Kutanthauza kuti pamene Kristu akhazikitsa ufumu ndi ulamuliro mumtima mwanu, ndiye kuti amakuchotseranichilakolakochauchimo kapena chilakolako cha moyo wokhumbachonyasa chilichonse. Kunena kuti Kristu amapereka m'phamvuyogonjetseramayesero, kuzunza ndi imfa zomwe zimadza ndi satana ndi ulamuliro wake pamoyo wanu ndi wanga.

Tsono chosangalatsa kwambiri muufumu umenewu, ndichakuti onse olowamuufumu uwu, adzakhalamokwamuyaya. Kutanthauza kuti ufumu wa Kristu ndi wamuyaya, koterokuti ngakhale

chiweruzo chotsirizasichidzakwanitsa kuchotsa ufumu umenewu. M'malo mwake chiweruzo chotsirizachi, chidzaonjezera kuonetsa ulemerero wa ufumu umenewu. Kunena kuti panthawi ya chiweruzo chimenechi, ndipo pamene mzinda watsopano wa Yerusalemu, udzaperekedwa kuchoka kwa Mulungu Kumwamba pamodzi ndi mpando wachifumu ndi Mwana wa Nkhosa alimomwemo. Iyi, ndinkhani yomwe akunena Yohane pa Chibvumbulutso 5:9, pamene akuti, “Ndipo ayimba nyimbo yatsopano ndi kunena, muyenera kulandira bukulo ndi kumasula zizindikiro zake; chifukwa mwaphedwa ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mapfuko onse ndi manenedwe onse ndi mitundu yonse.” Ndipo pa Chibvumbulutso 11:15, akutsindika kunena kuti, “Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri anaomba ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba ndi kunena Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu ndi wa Kristu wake: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi zanthawi.”

18.Kutha kwake kwachinthuchinkuno. Ine Danieli, maganizo anga anandibvuta kwambiri, ndi nkhope yanga inasandulika; koma ndinasungachithuchi m'mtima mwanga.

Pano Danieli akunena kuti uku ndi kutha kwake kwa zinthu zomwe adamva ndi kudziona. Ndiye akunena kuti zinthu zonsezi ndizomwe zinaperekedwakwa iye, kotero kuti anali kulingalira ndi chidwi pazinthu zonse zimene zinaonetsedwazo. Taonani mngelo akunena kuti, “kutha kwake kwa chinthuchinkuno.” Kutanthauza kuti ili ndilo bvumbulutso lomwe laonetsedwa kwa iye, kotero kuti zikhalira kwa iye kumalingaliramo ndi kusunga chinthu chimenechi. Kutsimikiza kuti Uthenga uliwonse umene waperekedwa kwa inu, Mulungu amayembekeza kuti mukhala ndi nthawi yolingalirapauthengawo kuti mumvetsetse cholinga chake pamoyo wanu ndi kukhalanawo pa inu nokha.

Ndiye taonani Danieli akunena kuti sichinakhale chinthu chachilendo kwa iye kuti Uthenga umenewu unamukhudza ayi. Kunena kuti zinthu zonse zomwe zinaonetsedwazo, zinali ndi zotsatira zake pamoyo wake. Kodi inu mumauona motere Uthenga wa Mulungu pamene ukuperekedwa kwa inu?

Tere, Danieli akunenetsa kuti zinthu zonse zomwe anazimva ndi kuona zinaupatsa maganizo akuti ndikoyenera kulingalira pa zinthu zomwe zinali mkudza. Mwanjira ina akunena kuti, kodi

alipo munthu amene akhoza kuona zatsogolo lake mopanda nkhawa? Ichi, ndichifukwa chake anali kulingalira ndichidwi kuti akhoza kupeza yankho kudzera mwazinthuzo. Tsono iyi, ndiyo nkhawa yomwe yohane anali nayo pa Chibvumbulutso 5:4, pamene anati, “Ndipo ndinalira kwambiri chifukwa sanapezedwa m’modzi woyenera kutsegulabukulo, kapena kulipenya.”

Ndiye tikunena kuti nkhawa imasintha maonekedwe a munthu. Kutanthauza kuti munthu wankhawasamasangalala, amasowa mtendere ndipo nkhope yake imakhala yoziya. Tere pomaliza Danieli akunena kuti anasunga mau onsewa kwa iye yekha kufikira pamene anaganiza kulemba mau amenewa. Kutanthauza kuti mtima wa munthu, uyenera kukhala nkhekwe yosungiramo zinthu za Mulungu. Ichi, ndichimene anachita Mariya pa Luka 2:51, pamene anati, “Ndipo amakeanasunga zinthu izi zonse mumtima mwake.” Kutanthauza kuti uthengawo unali wofunika kwambiri.

Tere Danieli anasunga zinthu zimenezi mumtima mwake, osati panali cholinga chakutiabisire anthu ena kapena kuti zisadziwikekumpingo ayi. Koma anali Kutanthauza kuti asunge ndi

cholinga chakuti zinthu zimenezi zidzagwiritsidwe ntchito kumpingo. Ichi, ndichifukwa chake anaganiza zolemba zinthu zonse zomwe anamva ndi kulandira kwa Ambuye, ndi cholinga chakuti azipereke kwa anthu a Mulungu mokhulupirika ndi moona.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, atumiki a Mulungu ayenera kukhala wokhudzidwa kukhala ndi chilakolakochozunga zinthu za Mulungu m'mitima mwawo pakukhala ndi nthawi yolingalirapamauwo, kuti akhoze kupereka uthengawo panthawi yoyenera. Kodi inu muli ndi chizolowezechosunga mau a Mulungu mumtima mwanu?

Kwalerotilekeza pano ndipo tinali kusanthula Danieli 7:14-28, momwe tinali kukambirana za kumasulira kwachirombochachinayi.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!